
4112

LESSONS FOR THE LIFE OF A CHRISTIAN (NYANJA)
PUBLISHED BY THE BAPTIST PUBLISHING HOUSE
PRINTED BY THE BAPTIST PRINTING MINISTRY
BOX 1995, LUSAKA, ZAMBIA

4117

# MAPHUNZIRO A MOYO WA MKRISTU

Part 1



ATnH
NyA

# LESSONS FOR THE LIFE OF A CHRISTIAN
(NYANJA)

FIRST PUBLISHED
JULY 1, 1978
BY THE
BAPTIST PUBLISHING HOUSE
P. O. BOX 1995
LUSAKA, ZAMBIA

PRINTED BY
THE BAPTIST PRINTING MINISTRY
P. O. BOX 1995
LUSAKA, ZAMBIA

ZOMWE PHUNZIRO IRI LITIPHUNZITSA IFE

1. Kupha munthu ndi cimo kwa Mulungu.
2. Chidano ndi cimonso kwa Mulungu.
3. Kusauza munthu za njira ya cipulumutso mwa Yesu ndi cimo.
4. Kusakhulululukira ena ndi cimo kwa Mulungu.

MAFUNSO:

1. Chulani njira zitatu zomwe anthu amaphera anthu ena.
2. Kodi lamulo lomwe taphunzira lero licokera m'buku liti?
3. Funsani munthu wina kuti anene mau apamtima alero.



4117

MAPHUNZIRO A MOYO WA MKRISTU

Olembedwa ndi:

Rev. Waddy Shibemba

Rev. Ackim Chali

Rev. and Mrs Leroy Albright

Rev. & Mrs Sam Sakala

Rev. & Mrs. Moses Chimfumpa

(Chairman & Advisor)

MAPHUNZIRO A SUNDAY SCHOOL


PHUNZIRO 1. KULEDZERA NDI MOWA............1

PHUNZIRO 2. KUDZIPEREKA...................5

PHUNZIRO 3. MPINGO NDI CIYANJANO CACE....8

PHUNZIRO 4. NCHITO YA MPINGO.............11

PHUNZIRO 5. CIGWIRIZANO CA MIPINGO......14

PHUNZIRO 6. CIMO LA KUKOKA FODYA........17

PHUNZIRO 7. KULEMEKEZA MULUNGU KUPYOLERA MKUYIMBA NYIMBO KULINGANA NDI CIPANGANO CATSOPANO.....23

PHUNZIRO 8. MULUNGU MMODZI YEKHA........27

PHUNZIRO 9. MAFANO......................31

PHUNZIRO 10. KULEMEKEZA DZINA LA MULUNGU.34

PHUNZIRO 11. KODI TSIKU LA KUPEMBEDZA MULUNGU NDI LITI?...........37

PHUNZIRO 12. KULEMEKEZA MAKOLO...........40

PHUNZIRO 13. USAPHE......................43


nchito. Akristu ambiri lero amapha anzawo kamba ka chidano m'mitima yawo. Werengani pamodzi m'buku la Mateyu 5:21-22. Lolani wina wa mkalasi lanu kuti awerenge m'buku la 1 Yohane 3:15.

Moyo uli mphatso ya Mulungu kwa ife. Tiri nayo mphamvu ya kuulandila koma tiribe mphamvu ya kuikanso moyo mwa munthu pomwe utatha. Njira ina imene anthu lero amaphera anzawo ndi ya kusalankhula kwa anthu ena pa za njira ya cipulumutso. Tiyeni tinene mnjira iyi mwacisanzo. Munthu wina anapita ku thengo tsiku lina kukapha nyama. Koma pamene anali kuthengo kuja anaona mkango. Mwamsanga anathawa nabwerera kumudzi wace. Tsono pamene anali kubwelera, anakomana ndi mnzace amene anali kupita ku thengoko kukapha nyama. Mnzace uja amene anali kucokera kuthengo sanamcenjeze za mkango uja ai. Anapitilira pa ulendo wace wakupita kumudzi. Tsono pamene munthu uja anafika kuthengo kuja mkango unabwera nudzadya munthuyo. Tsono tiyeni tione, colakwa, Kodi munthu uja anafa kamba ka ndani? Munthu uja anafa ndi mkango kamba ka mnzace uja amene sanamcenjeze za mkango ku thengoko.

Akristu ena lero amapha anthu ambiri. Iwo amadziwa mphoto ya cimo, koma samacenjeza anthu ena kuti acoke ku njira ya cimo ndi kubwera ku njira ya cipulumutso ya mwa Yesu Kristu. Lolani munthu m'modzi wa mkalasi lanu kuti awerenge m'buku la Ezekieli 33:8-9.

## USAPHE

MAU A MULUNGU: Eksodo 20:13

MAU APAMTIMA: *"Yense wakudana ndi mbale wace ali wakupha munthu; ndipo mudziwa kuti wakupha munthu aliyense alibe moyo wosatha wakukhala mwa iye."*

(1 Yohane 3:15)

MAU OYAMBA:

"Usaphe" iri ndi lamulo la Mulungu kwa munthu aliyense kuti alitsatire. Koma lero ciri cinthu codabwitsa pakuona kuti lamulo iri silitsatiridwa. Anthu lero ali kuphana mnjira zosiyana siyana. Ena anthu amapha anthu ena ndi mfuti, nyanga, ndi njira zina zoipa. Tsono mphunziro lathu lalero, tidzaona ciphunzitso ca Mulungu pa za kupha.

Mulungu anati "Usaphe" sanakambe za kusapha nyama za mthengo kapena mbalame. Koma kuti analankhula pa kusapha munthu cifukwa munthu analengedwa mcifaniziro cace. Inu tsopano monga mphunzitsi wa kalasi, lolani munthu m'modzi wa mkalasi lanu kuti awerenge m'buku la Genesis 9:1-3.

Tsopano tiyeni tione ziphunzitso za Yesu Kristu pa lamulo iri. Ciphunzitso ca Yesu ndi cakuti munthu aliyense amene amada m'bale wace ali munthu wa kupha. Yesu akuti munthu ayenera kucotsa chidano mumtima wace pa munthu wina. Ngati munthu ali ndi chidano mu mtima wace, Yesu sangamgwiritse





4117

## KULEDZERA NDI MOWA

MAU A MULUNGU: Miyambo 23:20; 23:29-31; Yesaya 5:11; Habakuku 2:15; 1 Akorinto 5:11; 6:9 ndi Aefeso 5:18.

MAU APAMTIMA: *"Usakhale mwa akumwaimwa vinyo, ndi ankhuli osusuka "*

(Miyambo 23:20)

MAU OYAMBA:

Mu Zambia monganso m'maiko ena, timapeza mitundu yosiyana siyana ya mowa. Mitundu ya mowa ina imapangitsa munthu kuledzera mwamsanga pamene ina siimatero. Anthu ambiri amafuna kumwa mowa womwe angathe kuledzera nawo. Anthu awa amati amapeza mtendere ndi cikondwerelo mu mowa, osati ico cokha, komanso timapeza Akristu ambiri amene amadzipereka ku kumwa mowa. "Mowa uli ngati cakudya ciri conse." Amatero. Kodi ici ciri coona motani? Lero tifuna kuti tipeze bvuto la pa za kumwa mowa.

MOWA UBWERETSA UMPHAWI - WERENGANI MIYAMBO 23:20-21!

Anthu ambiri mu Zambia akhala ali kulembedwa mumakampani amene ali kupeza ndalama zambiri zapadela ndipo apatsidwa malo anchito abwino. Ali kulipilidwa ndi ndalama zabwino kapena zambiri. Koma codabwitsa ndi cakuti, ngakhale kuti anthu awa amalandila ndalama zambiri izi amaononga ndalamazo

mwamsanga kamba ka kumwa mowa. Cifukwa ca ici, mabanja awo amakhala opanda cakudya ndi zobvala. Azimai ali oipa monganso amuna. Ngati apatsidwa ndalama za cakudya pa nyumba, amapita kukagula mowa. Mwamsanga kapena pambuyo pace amapeza kuti alibe ndalama. Tsono amayamba kukongola ndalama kwa anthu ena. Pakucita ici amaonjezela mabvuto ku mabanja awo. Kamba ka mkhalidwe uwu woipa pakati pa makolo, timaona kuti ana ambiri ali kubvutika kamba kosowa cakudya mu Zambia.

MOWA UBWERETSA KUSAUKA, CISONI NDI IMFA

Kodi ndi anthu angati amene tidziwa, amene anapezeka mu cisoni kubvutika kamba kakumwa mowa? Kumenyana pakati pa mwamuna ndi mkazi, kutha kwa zikwati, kulephera kugwira nchito, anthu ambiri akhala osoweka zinthu kamba kakumwa mowa. Ngati tidzapita ku cipatala tidzaona anthu amene apezeka mngozi kamba ka anthu amene amayendetsa magalimoto ndipo sasamala kuyenda bwino pa mseu, iwo amene amayendetsa magalimoto pomwe ataledzera ndi mowa. Werengani (Miyambo 23:29-32).

MPHUNZITSI: Lolani ophunzira anu kuti akambilane pa za kumwa mowa ndi zoturukamo zoipa mu mowa.

MOWA UMACOTSA MZIMU WOYERA MU MIYOYO YA AKRISTU AMBIRI

Pamene tilandila Yesu kukhala Mpulumutsi wathu, mathupi athu amakhala kacisi wa Mzimu Woyera. Werengani (1 Akorinto 6;19-20)



4. Ngati kulibe ulemu ndiye kuti sikungakhale mtendere.

5. Lamulo iri licokera kwa Mulungu ndipo mwana aliyense ayenera kulitsatira.

MAFUNSO:

1. Kodi lero taphunzira lamulo lotani?

2. Kodi zitsanzo zina ndi zotani **za pa** za ulemu?

3. Funsani munthu wina kuti anene ndime ya pamtima kopanda kuona m'buku.

4. Kodi ulemu uliko? Cifukwa?

5. Kodi lamulo pa za ulemu tilipeza m'buku liti?

6. Kodi inu ana mumalemekeza makolo anu?

ndapita kukaona "Kamdala" kapena "Kankhalamba" ai, koma kuti ndapita kukaona "Ambuye" kapena "Atate" kapena "Amai." Awa ayenera kukhala, maitanidwe anu a pa anthuwa. Monga inu mphunzitsi, talolani kuti m'modzi wa mkalasi lanu awerenge m'buku la 1 Timoteo 5:1-2. Tsono apa tiri kumva kuti tiyenera kulemekeza mwamuna mkuru monga tate, mkazi mkuru monga mai, mnyamata monga m'bale ndipo mtsikana monga mlongo wathu. Ngati aliyense adzatsatira kucita monga mau awa ndiye kuti tidzakhala pa mtendere pakati pa wina ndi mzace ndipo Mulungu adzakondwera ndi mkhalidwe wa mtundu uwu.

Mulungu analonjeza kuti ngati ana adzalemekeza makolo awo ndiye kuti masiku a moyo wawo pano pa dziko lapansi adzacuruka. Kodi tifuna kukhala ndi dziko la mphamvu? Tsono tiyenera kukhala ndi ana amene apereka ulemu ku makolo awo. Ana amene apereka ulemu ali ana abwino a dziko lathu la Zambia.

ZOMWE PHUNZIRO IRI LITIPHUNZITSA IFE:

1. Taphunzira kuti ciri cifuniro ca Mulungu kuti ana apereke ulemu ku makolo awo.

2. Kulemekeza makolo kuli kwa anthu enanso amene sali makolo athu.

3. Mulungu alonjeza kuti ngati ana adzalemekeza makolo awo Iye adzaonjeza masiku a moyo wawo pano pa dziko lapansi.



Tidziwa kuti Akristu ambiri amafuna Mzimu Woyera kubwera ndi kukhala mwa iwo. Koma pa nthawi yotereyi amafuna kumwa mowa. Buku Lopatulika litiuza poyera kuti izi ziwiri sizingayendelane pamodzi pa nthawi imodzi. Werengani Aefeso 5:18.

MOWA UDZALETSA ANTHU KUTI ASALOWE MU UFUMU WA MULUNGU

Ngakhale kuti tiri kukhala mdziko momwe tiganizira kuti kukondwera ndi cinthu comwe tifuna cabe, tsiku lidzabwera pomwe tidzafa. Ndi okhawo, anthu amene akhulupirira mwa Yesu Kristu monga Mpulumutsi wawo, amene adzaloledwa kulowa mu Ufumu wa Mulungu. Koma kwa iwo amene sanalandile Yesu Kristu monga Mpulumutsi wawo, akacita zoipa ndi kuledzera mowa sadzalowa mu ufumu wa Mulungu. Werengani 1 Akorinto 5:11 ndi 1 Akorinto 6:9.

KODI PHUNZIRO IRI LITIUZA KUTI TICITE CIANI?

1. Monga Akristu tiyenera kusiya cimo iri la kumwa mowa, ndi kukhala otsimikiza kuti mathupi athu akhala kacisi ya Mzimu Woyera.

2. Monga Akristu tiyenera kufunsa Mulungu kuti atipatse mphamvu ya kucitira umboni kwa iwo amene sali Akristu motero kuti akhulupilire mwa Yesu Kristu ndikuti asiye cimo la kuledzera ndi mowa.

MAFUNSO:

1. Kodi ndi cifukwa ninji Buku Lopatulika limaletsa kumwa mowa?

2. Kodi ciri cotheka kuti munthu akhale ndi moyo woyenera wa Cikristu ndi kumwańso mowa?

3. Kodi ndi macimo angati amene tingawerenge omwe tidziwa kuti anacokera kukuledzera ndi mowa? Chulani macimo a ang'ono.

MPHUNZITSI: Funsani ophunzira anu mafunso amene sanafunsidwe mphunziro iri pa za kuledzera ndi mowa kapena patsani mpata kwa ophunzira anu kuti afunse mafunso.



PHUNZIRO 12

## KULEMEKEZA MAKOLO

MAU A MULUNGU: Eksodo 20:13

MAU APAMTIMA: *"Ananu, mverani akukubalani mwa Ambuye, pakuti ici ncabwino."*

*(Aefeso 6:1)*

MAU OYAMBA:

Ulemu sicili cinthu cacilendo mdziko lathu la Zambia. Ulemu unayamba kale ndi azimbuye athu kapena makolo athu. Ulemu umathandiza kuonetsa mkhalidwe wabwino pakati pa- anthu. Banja kapena dziko lomwe liribe ulemu limakhala liribe mtendere. Limabweretsa manyazi ku maiko ena kapena ku mabanja ena.

Lero anthu amapereka ulemu kwa anthu ena kamba kakuti mwina anthuwo ali ndi cúma, kapena ali atsogoleri kapena ali akuru kwa iwo. Masiku ano timalemekeza m'busa ndi akuru ena mu chalichi kamba kakuti ali mtsogoleri. Ndipo anthu ena a m'boma kamba kakuti ali kutsogolera dzikoli.

Ndi cifukwa cace cirinso coyenera kuti ana ang'ono apatse ulemu ku makolo awo. Lolani m'modzi wa mkalasi lanu kuti awerenge Eksodo 20:12 ndi Aefeso 6:1.

Ulemu womwe ana ayenera kupereka ku makolo awo siuyenera kukhala ku makolo awo a mnyumba okha ai. Ana ayeneranso kupereka ulemu ngakhale kwa anthu ena amene ali akuru kupambana iwo. Siciri cabwino kunena kuti

4. Tsiku la Sabata liri lopatulika kwa Mulungu.

MAFUNSO:

1. Kodi tsiku la kupembedza Mulungu ndi liti chulani cifukwa cace tipembedza Mulungu pa tsikulo?

2. Ndi cifukwa ninji Mulungu anatipatsa tsiku la Sabata? Chulani zifukwa ziwiri.

3. Kodi mutu wa phunziro lathu lalero ndi uti?

4. Kodi lamulo lomwe taphunzira licokera m'buku liti?



PHUNZIRO 2

## KUDZIPEREKA

MAU A MULUNGU: Aroma 3:23; Yeremiya 31:29-33

MAU APAMTIMA: *"Ndinawabisa mau anu mumtima mwanga; kuti ndisalakwire Inu."*

*(Masalmo 119:11)*

MAU OYAMBA:

Ciri cinthu coona kuti munthu aliyense anacimwa naperewela pa ulemelero wa Mulungu. Cifukwa Buku Lopatulika linena kuti munthu aliyense anacimwa ndipo tonsefe tiri kusimikiza kuti tinacimwa, tiyenera kukhala acisoni ndi kucoka ku cimo ndi kubwera kwa Yesu ndi kumulandila iye kukhala Mpulumutsi wathu.

Lero tiri ndi bvuto pa za kudzipereka kwa munthu mwini kwa Yesu. Masiku ano anthu ena safuna kudzipereka iwo eni kwa Yesu cifukwa cakuti aganizira kuti makolo awo anawapereka iwo kwa Yesu motero kuti apulumutsidwe. Ici sicili coona. Munthu aliyense ayenera kubwera kwa Yesu mwa iye yekha osati kamba kakuti makolo anali kapena ali Akristu ai. Monga inu mphunzitsi, lolani munthu mmodzi wa mkalasi lanu kuti awerenge m'buku la Yeremiya 31:29-33.

Talolani tsopano ndi kuuzeni za nthano ya munthu wina amene anagwera mdzenje mwatsoka. Munthu wina anali pa ulendo wa kupita ku mudzi wina. Munthuyu anali ndi akatundu. Koma mwatsoka anagwera mu cidzenje cacitali kwambiri motero kuti sanathe kuturuka. Anakuwa mdzenje lija kupempha thandizo kwa anthu

ena amene anali kupita mnjira. Mwa mwai wina anabwera kudzamthandiza kuturuka mdzenje lija. Tsono munthu uja amene anali kubwalo kwa dzenje anamponyela chingwe kwa uja munthu yemwe anali mdzenje. Anamuuza kuti, uyenera tsopano kugwira ku chigwe ici. Akatundu ako onse amene uli nawo uyenera kusiya. Munthu uja anasiya akatundu ena koma akatundu ena anatenga ndipo anagwiririra ku chigwe. Munthu wakubwalo yemwe anali kumthandiza anayamba kukoka chigwe. Koma pamene anafika pakati ndi pakati chigwe cija cinaduka munthu uja yemwe anali ndi akatundu ace anagweranso mdzenje ndipo anafa.

Munthu uja anamva zonse zomwe winayo anamuuza kuti acite koma sanacite kulingana ndi mau ace. Akristu ena lero amacita cimodzi modzi ndi zomwe munthu uja yemwe anagwera mdzenje anacita. Anthu ambiri lero amabwera kwa Yesu Kristu ndi kukhala Akristu. Koma safuna kusiya akatundu awo. Angakhale katundu wa kumwa mowa, katundu wa cigololo, katundu wakuba zinthu za eni, katundu wakukoka camba ndi akatundu ena ace. Njira yabwino yakudzipereka kwa Yesu ndi ya kusiya akatundu onse oipa amene tiri nawo. Ngati titero, ndiye kuti tidzakhala anthu olengedwa atsopano mwa Yesu Kristu. Lolani munthu mmodzi kuti awerenge 2 Akorinto 5:17.

Pamene munthu adzipereka kwa Yesu nakhala Mkristu iye amakhala ngati mwana wobadwa m'banja la Mulungu. Ciyenereka kwa iye tsono kuti akule mu mzimu ndi mcikhulupiriro. Iye ayenera kuwerenga Buku Lopatulika ndi kupita ku chalichi ku mapemphero sabata liri lonse.



tsa tsiku limeneli. Mulungu anatipatsa tsiku-li motero kuti tipume kucokera ku nchito zathu ndi kupembedza Mulungu.

KUSINTHA KWA TSIKU

Tsopano tiyeni tione kasinthidwe kace ka tsiku lakupembedza. Akristu ambiri lero ali kupembedza Mulungu pa tsiku loyamba la Sabata m'malo mwa tsiku la cisanu ndi ciwiri. Ici cinasinthidwa kamba ka kuuka kwa Ambuye Yesu pa tsiku loyamba la Sabata. Cifukwa cina ndicakuti, ophunzira a Yesu Kristu anatsogoleredwa ndi Mzimu Woyera kukumana pa tsiku loyamba la Sabata. Lolani kuti munthu m'modzi wa mkalasi lanu awerenge m'buku la Macitidwe 20:7.

Ciri cofunikira kuti Mkristu aliyense apite ku chalichi pa tsiku loyamba la Sabata ndi kupembedza Mulungu. Cirinso coyenera kuti Mkristu aliyense apite ku chalichi motero kuti akhale mciyanjano ndi Akristu ena.

ZOMWE PHUNZIRO IRI LITIPHUNZITSA:

1. Tsiku la Sabata linapatsidwa kwa munthu aliyense monga mphatso kucokera kwa Mulungu.

2. Tsiku la Sabata linapatsidwa kwa ife motero kuti tipume ndi kupembedza Mulungu.

3. Kusintha kwa tsiku la Sabata kunacitika kamba ka kuuka kwa Yesu.

MPHUNZITSI: Funsani ophunzira anu kuti alankhule pa njira zomwe ziri zoipa. zomwe ziyenera kukonzedwa motero kuti machalichi athu aphunzire kupereka ulemu kwa Mulungu.

## PHUNZIRO 11

## KODI TSIKU LA KUPEMBEDZA MULUNGU NDI LITI?

MAU A MULUNGU: Eksodo 20:8-11

MAU APAMTIMA: *"Ndipo anawauza, nao, Sabata linaikidwa cifukwa ca munthu, si munthu cifukwa ca Sabata."*

*(Marko 2:27)*

MAU OYAMBA:

Mphunziro lathu lalero tidzaphunzira za ndi cifukwa ninji Mulungu anatipatsa tsiku la kupembedza. Mkati mwa phunziro tidzaphunziranso za kasinthidwe ka kupembedza tsiku loyamba la Sabata m'malo mwa tsiku la cisanu ndi ciwiri.

Mulungu anapatsa malamulo khumi kwa anthu kuti atsatire mu miyoyo yawo. Lamulo limodzi mwa malamulo khumi Mulungu adati: "Kumbukirani tsiku la Sabata kuti liri lopatulika kwa Mulungu." (Lolani m'modzi wa mkalasi lanu kuti awerenge Eksodo 20:8-11). Mulungu anatipatsa tsiku la sabata monga mphatso kwa ife. Tsono tiyeni tione mwatsatane tsatane ndi cifukwa ninji Mulungu anatipa-



## ZOMWE PHUNZIRO IRI LITIPHUNZITSA

1. Aliyense anacimwa.
2. Munthu aliyense ayenera kusankha pa za cipulumutso mwa Yesu Kristu.
3. Munthu aliyense alape macimo ace nabwera kwa Yesu Kristu.
4. Munthu ayenera kukula Mcikristu cace pa kuwerenga Buku Lopatulika ndi kupita ku chalichi.

MAFUNSO:

1. Kodi ndi anthu oti amene anacimwa?
2. Kodi liu lakuti "kutembenuka" litanthauza ciani?
3. Kodi lero munthu akhoza kupulumutsidwa kamba kakuti makolo ace ali kapena anali Akristu?
4. Kodi Mkristu adzakula Mcikristu cace mnjira zotani?
5. Kodi ndi Buku liti limene litiuza kuti munthu aliyense anacimwa?

PHUNZIRO 3

## MPINGO NDI CIYANJANO CACE

MAU A MULUNGU: Macitidwe 2:44-47

MAU APAMTIMA: *"Osaleka kusonkhana kwathu pamodzi, monga amacita ena, komatu tidandaulirane, ndiko koposa monga momwe muona tsiku lirikuyandika."*

*(Ahebri 10:25)*

MAU OYAMBA:

Colinga ca phunziro iri ndi kupeza zinthu zina zomwe mpingo ungathe kucita motero kuti ubweretse ciyanjano pakati pa anthu. Coyamba tiyeni tione tanthauzo la mpingo. Kodi mpingo ndi ciani? Mpingo ndi guru la anthu amene ali okhulupiririka kwa Yesu osati nyumba ya kupempherera mo ai. Tiyeni tipezenso tanthauzo la ciyanjano. Ciyanjano citanthauza anthu amene agwira nchito yonse mogwirizana.

Masiku ano, mpingo ukhoza kubweretsa ciyanjano pakati pa anthu mnjira zosiyana siyana. Mwacitsanzo, pa nsaka pomwe anthu a m'mudzi amabweretsa cakudya nadya pamodzi cakudyaco. Akristu lero akhoza kucita cimodzi modzi. Akhoza kubweretsa zakudya zawo pa malo amodzi ndi kudya ndi Akristu anzawo. Lolani mmodzi wa mkalasi lanu kuti awerenge m'buku la Macitidwe 2:46-47.

Cinthu cinanso comwe cingabweretse ciyanjano pakati pa anthu mu mpingo ndi cigwirizano ca azimai kapena misonkhano ya azimai. Pamene azimai amabwera ku chalichi



lace pa cabe. Werengani Mateyu 5:34-35. Kulankhula cabe dzina la Mulungu sikuli kokwanila kuti kungathandize kutsogolera munthu aliyense ku cipulumutso. Koma kucita cinthu comwe Mulungu afuna cikhoza kupulumutsa moyo wa munthu. Mateyu 7:24.

## M'MENE TINGALEMEKEZELE DZINA LA MULUNGU

Mulungu afuna ife kuti tilemeke ndi kutamanda dzina lace. Tikhoza kubweretsa ulemu ku dzina lace kupyolera mzimene ticita. Monga Akristu tiyenera kubweretsa ulemu kwa iye mzinthu zonse zomwe ticita. Izi ndi zisanzo zing'ono:

1. Tikhoza kubweretsa ulemu kwa Mulungu m'manyumba athu pamene tiphunzitsa ana athu.
2. Ana ayenera kudziwa m'mene angaperekere ulemu kwa Mulungu pa nthawi ya misonkhano ya mapemphero ndi pomwe tiri mchalichi ndi anthu ena kupembedza Mulungu. Tiyenera kulemekeza dzina lace nthawi zonse.

MAFUNSO:

1. Kodi ndi zinthu zotani zomwe tingacite motero kuti Akristu anzathu apereke ulemu ku dzina la Mulungu?

2. Kodi tingakonze bwanji mapemphero a pa sabata motero kuti dzina la Mulungu lilemekezedwe?

M'maiko ambiri, anthu amene apezeka kuti alikuyipitsa maina a atsogoleri amaperekedwa ku khoti la ciweruzo. Mphunziro iri, tidzaphunzira za m'mene tingabweretsere ulemu ku dzina la Mulungu amene ali ndi mphamvu pa mafumu onse ndi atsogoleri a dziko lapansi.

## DZINA LA MULUNGU

Dzina la Mulungu liri Lopatulika. Liri dzina lomwe lipambana maina onse. Palibe dzina lina pano pa dziko lapansi lomwe lipambana dzina la Mulungu. Conco, dzina lace cabe, liyenera kulemekezedwa.

## M'MENE TINGALANKHULIRE DZINA LA MULUNGU

Ambiri amakōnda kutenga dzina la Mulungu mwacabe. Amalankhula pa za dzinali mnjira za cabe. Nthawi zina pamene anthu apangana pa cinthu coipa monga kuba, kupha, ndi ufiti, amalankhula dzina la Mulungu ndipo amalumbila ndi dzinalo.

Ena pakuona kulangidwa ku khoti pa nthawi ya ciweruzo, amafuna kulumbila ndi dzina la Mulungu ndi kulankhula bodza zina zace motero kuti asaikidwe mndende. Cifukwa ca nzeru iyi, Mulungu anapereka lamulo iri ku ana a Israyeli (Eksodo 20:7) kukhuza pa za tsoka la kutenga dzina lace mwa cabe.

MPHUNZITSI: Funsani ophunzira anu kuti achule zinthu zoipa momwe anthu amakonda kutenga dzina la Mulungu mwa cabe. Mulungu ali kuticenjeza kuti sitiyenera kuchula dzina



pamodzi cimathandiza mzimai aliyense kukhala mciyanjano ndi azimai ena.

Cinthu cina comwe cingabweretse ciyanjano pakati pa anthu mu mpingo ndi cigwirizano mnchito. Mwacisanzo, mumzinda, ngati chalichi iribe magalasi mumadzenela anthu akhoza mciyanjano kusonkha ndalama kuti agule magalasi. Ndipo akhoza kubwera ku chalichi kudzafesa maluwa, ndi zina zace zambiri zomwe akhoza kucita ndi manja awo.

Ngati tibwera kumbali ya m'midzi, anthu mciyanjano akhoza kulima munda wa chalichi pamodzi kapena dimba la ndiwo za masamba. Ndipo anthu a mu mpingo akhoza kuthandiza ena amene afuna thandizo. Monga anthu okalamba ayenera kuthandizidwa ku zobvala. Ku watungilako madzi ndi kuwaphikilako cakudya ndi kusesa munyumba.

Cirinso cinthu coyenera kwa Akristu kuti azicezera anthu ena mmakhomo. Ayenera kuwakonda iwo ndi kuwathandiza zinchito zawo. Mphunzitsi, tsopano lolani mmodzi wa mkalasi lanu kuti awerenge Ahebri 10:24.

Akristu ayenera kudya cakudya cawo pamodzi ndi ena m'manyumba awo nthawi zina. Akristu akuda ndi Akristu azungu ayenera nthawi zina kudya pamodzi mciyanjano. "Mlendo wa fulu amadya cakudya comwe fulu amadya." Ici citanthauza kuti simuyenera kubvutika kufunafuna zakudya zabwino kupambana zomwe muli nazo pamene munthu wacuma kapena mzungu aitanidwa kubwera kunyumba yanu.

ZOMWE PHUNZIRO IRI LITIPHUNZITSA

1. Taphunzira kuti mpingo si nyumba ai, koma anthu amene ali obatizidwa ndipo ali okhulupirika kwa Yesu.

2. Mpingo uyenera kupereka ciyanjano cabwino pakati pa anthu.

3. Tiyenera kukhala ndi cifuno cakukhala mciyanjano mu mpingo, pa nchito ndi mmanyumba.

MAFUNSO:

1. Kodi mpingo ndi ciani?

2. Kodi ciyanjano ndi ciani?

3. Chulani njira zinai zomwe mpingo ukhoza kuperekera ciyanjano pakati pa anthu.

4. Funsani munthu wina kuti anene mau apamtima kopanda kuyangana m'Buku Lopatulika.

5. Kodi mutu wa phunziro lathu lalero ndi uti?



Mpulumutsi wathu, Mulungu afuna ife kuti tisiye kupembedza mafano. Tiyenera kusiya cinthu ciri conse comwe cingakhale fano kwa ife ndipo tiyenera kukhala ophunzira okhulupirika a Yesu Kristu.

Mkalata ya Yohane yoyamba kwa ife, ali kutiuza molimba kuti ticoke kukupembedza mafano. Werengani 1 Yohane 5:20-21. Mphunzitsi ayenera kufunsa ophunzira ace kuti akambilane pa za mafano amene iwo ayenera kucokako.

MPHUNZITSI: Patsani ophunzira anu nthawi ya kufunsa mafunso.

PHUNZIRO 10

KULEMEKEZA DZINA LA MULUNGU

MAU A MULUNGU: Eksodo 20:7; Mateyu 5:34-35 Mateyu 6:9

MAU APAMTIMA: *"Usachule dzina la Yehova Mulungu wako pacabe; cifukwa Yehova sadzamuyesa iye wosacimwa, amene achula pacabe dzina lacelo."*

*(Eksodo 20:7)*

MAU OYAMBA:

Pamene mafumu ndi atsogoleri ena amadziwika kwambiri, anthu amayesa yesa kubwera kwa iwo ndi ulemu. Ciri cinthu ca manyazi kukamba dzina la munthu woyenera mwa cabe cifukwa kutero sikupatsa ulemu wace.

pambuyo pace. Cinthu ciri conse comwe cimatenga nthawi ya Akristu ambiri m'miyoyo yawo cimakhala fano. Amakhala ali kugwiritsa nthawi yawo pa kuwerenga manyuzi pepala m'malo mwa kuwerenga Buku Lopatulika ndi kupemphera. Ena amafuna kupita ku malo a masewela mmalo mwa kupita ku chalichi pa tsiku loyamba la Sabata. Mbari ina ku ndalama kupambana Mulungu. Kulinso zinthu zina zambiri zomwe Akristu amapitako ndi kuzipanga kukhala mafano mu umoyo wawo wonse.

KODI MULUNGU ALANKHULA ZOTANI POMWE ANTHU ACE APEMBEDZA MAFANO?

Mulungu amakalipa. Ndi cifukwa cace amalankhulabe kuti anthu ace ayenera kucoka ku kupembedza mafano. Pamene ana a Mulungu amayamba kupembedza mafano amaleka kupembedza Mulungu wawo ndi kutamanda dzina lace Werengani Eksodo 32:1-4.

Mulungu amamva nsanje pomwe ana ace amapita kutali kucokera kwa iye ndi kupanga milungu ina yochedwa mafano. Conco, ife Akristu, tiyenera kusiya kupereka nthawi yathu ku mafano m'malo mwa Mulungu. Werengani Eksodo 20:3-4. Mulungu ndiye Ambuye wa moyo wathu, ndipo safuna kupereka ulemelero wace ku zinthu zina monga mafano. Werengani Yesaya 42:8.

AKRISTU AYENERA KUCOKA KUKUPEMBEDZA MAFANO

Moyo wa Mkristu ndi moyo wozipereka Pomwe tatha kulandila Yesu Kristu monga



PHUNZIRO 4

NCHITO YA MPINGO

MAU A MULUNGU: Mateyu 28:19-20

MAU APAMTIMA: *"Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezero ace a dziko."*

*(Macitidwe 1:8)*

MAU OYAMBA:

Lero m'phunziro lathu tidzakhala tiri kuona nchito yomwe mpingo uyenera kucita. Ndi zoona kunena kuti mutu wa mpingo ndi Yesu. Yesu Kristu ali payo mphamvu ya kulamulira mpingo wace ndi kuutsogolera. Kopanda utsogoleri wa Yesu mpingo siungathe kucita ciri conse.

Pamene Yesu Kristu asanapite kumwamba analamulira ophunzira ace kugwira nchito ya kupita mdziko lonse ndi kupanga anthu kukhala ophunzira ace, kubatiza iwo mdzina la Atate ndi Mwana ndi Mzimu Woyera. Nchito iyi iri ya mpingo kucita. Kulalikira ndi kuphunzitsa anthu nthawi zonse ngakhale pamene anthu atabatizidwa ayenerabe kuphunzitsidwa motero kuti akule mu mzimu. Mpingo siuyenera kuleka kuphunzitsa anthu mau a Mulungu cifukwa iri ndi lamulo la Yesu. Mphunzitsi, lolani munthu wina wa mkalasi lanu kuti awerenge m'buku la Mateyu 28:19-20.

Lamulo lina lomwe Yesu anapereka ku mpingo kuti ucite ndi "Kuyanganira mgonero

wa Ambuye." Mipingo yambiri amakhala awa nthawi yaitali kopanda kudya mgonero wa Ambuye, uku ndi kulakwa. Yesu Kristu anati mpingo uyenera kucita ici kufikira acabwera Iye. Lolani munthu m'modzi kuti awerenge m'buku la 1 Akorinto 11;24-26.

"Inu ndinu mboni zanga" awa anali mau a Yesu kwa ophunzira ace pomwe asanapite kumwamba. Mau awa ali kwa membala aliyense wa mu mpingo. Membala aliyense ayenera kucitira umboni Yesu Kristu kuli konse komwe ali kapena kuli konse komwe amapita. Anthu ena lero ali ofoka kucitira umboni Yesu Kristu cifukwa samudziwa bwino iwo eni. Kodi inu mumamdziwa Yesu Kristu? Kodi mumamcitira umboni Iye kwa anthu ena amene mukhala nawo kapena amene mukomana nawo? Akristu onse lero ayenera kuphunzira lamulo iri la kucitira umboni Yesu Kristu kwa anthu ena motero kuti apeze cipulumutso mwa iye. Mphunzitsi lolani munthu m'modzi wa mkalasi lanu kuti awerenge m'buku la Macitidwe 1:8.

Cinthu cinanso ndi cakuti, iri nchito ya mpingo kuyamba mipingo ina m'madela ena. Siiri nchito ya amishoni okha ai koma kuti amishoni ndi mpingo uli wonse uyenera kuyamba mipingo yatsopano. Kuli malo ambiri amene kulibe mipingo. Mipingo iyenera kupita ku maiko enanso ndi kupereka Uthenga wa Yesu Kristu.

ZOMWE PHUNZIRO IRI LITIPHUNZITSA

1. Litiphunzitsa kuti Yesu analamulira mpingo wace kupanga ophunzira ace,



MPHUNZITSI: Mukhoza kuonjezera ku mafunso awa kapena mukhoza kulola ophunzira anu kufunsa mafunso kulingana ndi phunziro iri.

PHUNZIRO 9

MAFANO

MAU A MULUNGU: Eksodo 20:3-4; 32:1-4, Yesaya 42:8 ndi 1 Yohane 5:20-21

MAU APAMTIMA: *"Tiana, dzisungireni nokha kupewa mafano."*

*(1 Yohane 5:21)*

MAU OYAMBA:

Mdziko lino la Zambia, nthawi zina timapeza ndalama zopangidwa zomwe siziri ndalama zoona ai. Ndipo ndalamazi m'maonekedwe zimaoneka kuti ziri ndalama zeni zeni zomwe boma linalola. Anthu amene amapanga ndalamazi amatero motero kuti azigwiritse nchito. Mwa soka, iwo amene amapezeka kugwiritsa nchito ndalamazi amaperekedwa ku bwalo la milandu kamba kakukhala osakhurupirika. Mphunziro iri tidzafuna kuona ndi cifukwa ciaji Mulungu safuna kapena kulola kuti anthu asapembedze mafano kapena zinthu zina zace.

1. KODI NDI MITUNDU YOTANI YA MAFANO YOMWE ANTHU AMAPEMBEDZA?

Anthu ambiri a Cikristu amapatsa malo oyamba mmiyoyo yawo ku zinthu zomwe zimasandurika mafano

munthu kupyolera mu mwana wace Yesu Kristu. Werengani Yesaya 9:6 ndi Mateyu 1:23. Monga ife Akristu, tiyenera kulandila Yesu ndi kumpembedza iye monga Mulungu mmodzi yekha. Sitiyenera kupembedza milungu ina yomwe ingathe kucinjiriza ife kukhala mciyanjano pamodzi ndi Mulungu ndi Yesu kuti tisakule kukhala olimba. Werengani Mateyu 6:24. Mateyu 6:24 itiuza kuti sitingathe kutumikira ambuye awiri pa nthawi imodzi.

KODI PHUNZIRO IRI LITIUZA KUCITA CIANI?

1. Monga Akristu tiyenera kubvomeleza kuti kuli Mulungu mmodzi yekha.

2. Mulungu mmodziyu ndiye amene akhala munthu kupyolera mu mwana wace Yesu Kristu.

3. Ife amene tiri Akristu, ngati ticimwa ndi kuthawa kucokera kwa Mulungu, tiyenera kudziwa kuti tsopano tiri kuzipangila mafano athu eni ndi kupita ku milungu ina imene mulibe moyo.

MAFANSO:

1. Kodi ndi maganizo otani amene munthu angakhale nawo, omwe pambuyo pace akhoza kukhala milungu ina?

2. Kodi Mulungu amakondwera naco pamene munthu atenga cinthu cina cace mmalo a Mulungu?



kuwabatiza ndi kuwaphunzitsa.

2. Taphunzira kuti munthu aliyense ali mboni ya Yesu Kristu.

3. Taphunzira kuti mipingo iyenera kukhala ndi nchito ya kupanga machalichi ena.

4. Ndipo mpingo uyenera kuyanganira mgonero wa Ambuye.

MAFUNSO:

1. Kodi ndi malamulo angati kulingana ndi phunziro lathu amene Yesu analamulira kuti mpingo ucite?

2. Kodi ndani mboni za Yesu lero?

3. Ndani amene ayenera kuyamba mipingo yatsopano?

PHUNZIRO 5

## CIGWIRIZANO CA MIPINGO

MAU A MULUNGU: 1 Akorinto 12:12-26

MAU APAMTIMA: *"Sindikhalanso m'dziko lapansi, koma iwo ali m'dziko lapansi, ndipo Ine ndidza kwa Inu. Atate Woyera, sungani awa m'dziko lanu amene mwandipatsa Ine, kuti akhale mmodzi monga ife."*

*(Yohane 17:11)*

MAU OYAMBA:

Lakhala bvuto lalikuru pakati pa mipingo yathu ya Baptist kamba ka liu lakuti "Ufulu." Mipingo ina yathu yakhala iri kukana utsogoleri wa Yesu Kristu kamba ka liu limeneli.

Pamene Yesu akhala mutu wa mpingo. Iye amakhala mutu wa mipingo yonse ya a Baptist mu Zambia. Motero mpingo uli wonse wa Baptist siuli wa ufulu koma kuti usamila pa Yesu. Ici ndi cifukwa cakuti tonsefe tiri m'banja limodzi la Yesu. Ife tonse tiri ana a Mulungu. Mphunzitsi lolani mmodzi wa mkalasi lanu kuti awerenge m'buku la Yohane 1:12.

Thupi limodzi ndi ziwalo zambiri: Ngakhale kuti thupi liri ndi ziwalo zambiri, ziwalo zonse zimagwira nchito mwa mphamvu pamodzi mogwirizana. Kulibe ciwalo comwe cinganene kuti sindifuna kugwirizana ndi ziwalo zina. Ici ndi cimodzi modzi ndi mpingo wa Yesu Kristu. Mpingo wa Yesu



Ana a Israyeli anali akapolo mu Aigupto. Pamene anali mu Aigupto anapembedza milungu yambiri. Cinali capafupi kwa iwo kuti apembedze milungu iyi. Kamba ka cifukwa ici, Mulungu anapereka lamulo kwa ana a Israyeli kuti asunge ndipo acoke kukupembedza mafano. Anali kuyembekezedwa kuti akhale ndi Mulungu mmodzi yekha, amene anawamasula kucokera ku ukapolo (Werengani Eksodo 32:1-4).

Monga Akristu tiri cimodzi modzi monga ana a Israyeli. Ana a Israyeli anali mu ukapolo mdziko la Aigupto monganso ife tinali mu ukapolo wa cimo ndi mdielekezi. Pamene tikhulupirira mwa Yesu monga Mpulumutsi wathu, tiyenera kusiya kupembedza milungu ina ndipo tiyenera kutsatira Yesu mwanthunthu. Tiyenera kusiya milungu ina yomwe tinadziwa kale pomwe sitinakhale otsatira a Yesu Kristu.

### KODI MULUNGU MMODZI YEKHAYU NDANI?

Ndi mulungu mmodzi yekha, amene analenga zinthu zonse zomwe tiri nazo mdziko lapansi. Analenga thambo lakumwamba, dziko lapansi ndi munthu. Anaonekela kwa Abrahamu, Isake ndi Yakobo. Anaonekelanso kwa Mose pamene anabwera kudzamasula kucokera ku ukapolo mu Aigupto. Ndiye Mulungu yekha mmodzi. Kulibe Mulungu wina wace kupambana Iye. Werengani Masalmo 83:18 ndi Yesaya 43:10-11.

### MULUNGU YEKHA MMODZIYU ANAKHALA MUNTHU KUPYOLERA MWA YESU

Pamene anatha kuzibvumbulutsa yekha ana a Israyeli, Mulungu yekha mmodziyu anakhala

PHUNZIRO 8

## MULUNGU MMODZI YEKHA

MAU A MULUNGU: Eksodo 20:3; Masalmo 83:18 Yesaya 43:10-11,; Marko 12:29 Yohane 1:1-2 ndi 1 Akorinto 8:4.

MAU APAMTIMA: *"Yesu anayankha, kuti, La m'[illegible] ndili, Mvera, Israyeli; Ambuye Mulungu wathu, Ambuye ndiye mmodzi."*

*(Marko 12:29)*

MAU OYAMBA:

Pamene mwamuna akwatira mkazi, amafuna kuti akhale wa iye yekha. Mkazi nayenso amafuna kuti mwamuna akhale wa iye yekha nayenso. Cingakhale cinthu comvetsa manyazi kwambiri kwa mwamuna kuyenda ndi akazi ena mwa cinsinsi. Ndi cimodzi modzi ndi mkazi amene ali okwatira kale.

Munthu amene akhulupirira mwa Yesu Kristu monga Mpulumutsi wace ali ngati munthu wokwatira. Iye ayenera kukhala ndi kuyenda ndi Yesu Kristu ndi kumpanga Iye monga Mulungu wace mmodzi yekha. Sayenera kugawanitsa cikondi cace kuti cina cipite kwa Mulungu ndiponso cina kwa Satana. Mphunziro iri tidzafuna kuti tiphunzire za mmene tingakhalile kutsata Mulungu yekha mmodzi.

NDI CIFUKWA NINJI MULUNGU ANAFUNA KUTI ANA A ISRAYELI ASANKHE NDI KUTSATA IYE MONGA MULUNGU MMODZI YEKHA



siuyenera kunena kuti sindidzagwirizana ndi mipingo ina. Mphunzitsi, lolani munthu m'modzi wa ophunzira anu kuti awerenge m'buku la 1 Akorinto 12:12-26. Apa tiri kuuzidwa povera kuti mu mpingo wa Yesu simuyenera kukhala ndi mikangano ai koma kukhala omvera ndi kugwirizana. Ngati mpingo wina uli m'mabvuto mipingo yonse imakhala m'mabvuto. Ngati mipingo ina iri mokondwelero mipingo ina imakhala yokondwera. Werengani 1 Akorinto 12:25-26.

Lero tiri ndi zigwirizano ziwiri zochedwa Assosiyenshoni ndi Konvenshoni. Colinga ca zigwirizano izi ndi kufuna funa njira yomwe tingaperekeremo Uthenga wa Yesu ku malo akutali komwe mpingo umodzi siungathe. Monga mudziwa kuti "Cala cimodzi sicingathe kutenga nsabwe."

Mipingo yonse iyenera kuthandiza kupereka ndalama ku Assosiyenshoni ndi Konvenshoni motero kuti nchito ya mzigwirizano zimenezo zicitike. Ciri cinthu cofunikila kuti anthu a m'mipingo ayenera coyamba kuzipereka iwo okha kwa Mulungu motero kuti angathe kupatsa ndalama zawo ku Assosiyenshoni ndi ku Konvenshoni. Lolani munthu m'modzi kuti awerenge m'buku la 1 Akorinto 8:5.

ZOMWE PHUNZIRO IRI LITIPHUNZITSA

1. Palibe mpingo womwe uli pa okha koma kuti uli kusamala pa utsogoleri wa Yesu.

2. Mutu wa mpingo ndi Yesu Kristu.

3. Cigwirizano pakati pa mipingo ya Yesu ciri cofunikira.

4. Ma Assosiyenshoni ndi Konvenshoni zonsezi ziri za mipingo.

5. Mipingo iyenera kupereka ndalama ku Assosiyenshoni ndi ku Konvenshoni.

MAFUNSO:

1. Kodi ndi njira iti yomwe mipingo ingathe kugwira nchito pamodzi?

2. Kodi mpingo wanu umapereka ndalama ku Assosiyenshoni ndi ku Konvensoni?

3. Kodi mpingo wanu ugwirizana ndi mipingo ina.

4. Kodi mau athu apamtima akuti ciani?



4. Tikhoza kulalikira Uthenga wa Mulungu kupyolera mkuyimba nyimbo.

MAFUNSO;

1. Kodi timayimba mu mzimu wacikondwerero pamene tiri mu mpingo?

2. Kodi mamembala a khwaya yathu amadziwa ndi cifukwa ninji kapena cimene ayimbira?

MPHUNZITSI: Mukhoza kufunsa mafunso ena kapena kulola ophunzira anu kuti akufunseni mafunso ocokera mphunziro iri.

NYIMBO MNCHITO YA ULALIKI WA PAULO

Kuyimba kwa Paulo ndi Sila mndende, kutionetsa zomwe Akristu angacite mnthawi ya mabvuto. Potsilizira, wosunga a ndende anakhulupilira mdzina la Yesu Kristu. Banja lace nalonso linacita cimodzi modzi.
KAMBILANANI: Kodi tingathe kuyimba pamene tiri m'mabvuto?

NYIMBO KUMWAMBA:

Kuyimba nyimbo zotamanda Mulungu sikuzacitika pa dziko lapansi cabe, koma kuzapitirirabe ngakhale kumwamba. Sitidziwa m'mene tidzayimbila, koma tiri oona kuti kuyimba kudzakhalako. M'buku la Cibvumbulutso tiwerenga kuti okhulupirika a Yesu adzayimba nyimbo zotamanda Mulungu. Werengani Cibvumbulutso 15:3-4; 7:9-19.

KODI PHUNZIRO IRI LITIPHUNZITSA ZA CIANI?

1. Litiphunzitsa kuti kuyimba kwa nyimbo kuli koyenera kwambiri mu moyo wa Cikristu ndi mpingo.

2. Pamene tiyimba tiyenera kupereka ulemelero kwa Mulungu.. Sitingathe kuyimba mopanda colinga, ici cikhoza kukhala ciribe tanthauzo kwa ife ndi kwa Mulungu.

3. Pamene tiri m'mabvuto kapena pomwe tiri mcikondwerero tikhoza kuyimba nyimbo zotamanda Mulungu.



PHUNZIRO 6

CIMO LA KUKOKA FODYA

MAU A MULUNGU: Yesaya 55:7; Aroma 12:1; 1 Akorinto 6:19-20.

MAU APAMTIMA: *"Woipa asiye njira yace, ndi munthu wosalungama asiye maganizo ace, nabwere kwa Yehova; ndipo Yehova adzamcitira cifundo; ndi kwa Mulungu wathu, pakuti Iye adzakhululukira koposa."*
*(Yesaya 55:7)*

MAU OYAMBA:

Kulingana ndi moyo wa pano pa dziko lapansi womwe tiri nawo, umoyo wathu usamila pa cakudya comwe timadya. Nsima ndi cakudya cathu ca tsiku ndi tsiku kulingana ndi mwambo, ndi cakudya colimba comwe cilimbitsa thupi mdziko lathu la Zambia.

Komanso, tiri ndi zakudya zina monga chinangwa, mbatata, dzungu ndi zina zace zambiri. Mathupi athu amakula pamene apatsidwa zakudya izi ndi kuti zilimbitsa thupi ndi kupereka mphamvu. Codabwitsa cina ndi ici, kuli zakudya zina zosiyana siyana zomwe siziri zabwino kwa ife ndipo sizimapereka thandizo liri lonse kukakulidwe ka thupi koma kuononga cabe mathupi. Kukoka fodya mnjira iri yonse ndi cinthu cimodzi ca zoipazo.

KODI FODYA CIRI CAKUDYA CABWINO?

Pakufunsa anthu amene amakoka fodya pa za nkhaniyi, amatiuza kuti, kulibe cabwino mkukoka fodya. Cifukwa cimodzi comwe apereka

ndi cifukwa ca "udzu" comwe amapeza mu fodya. Nthawi zambiri madotolo amapereka phunziro pa za kuipa kwa fodya ndipo amapereka cenjezo kwa odwala kuti ayenera kusiya kukoka fodya. Amatero cifukwa amadziwa kuti fodya amabweretsa matenda ku mapwapwa a munthu pakukoka fodya uli wonse. Matenda awa nthawi zina amabweretsa imfa. Buku la Yesaya limaticenjeza ife kusagwiritsa ndalama zathu pa zinthu zosayenera. Werengani Yesaya 55:7. Lankhulani pa za cinthu ciri conse cimene mwapeza cabwino pa iwo amene akoka fodya.

KULI MITUNDU YAMBIRI YA FODYA

I. Fodya wopela wa Mphuno.

Mtundu wa fodya uyu ugwiritsidwa nchito mu Afrika maka maka. Okoka fodyawu amaika mphuno zawo cifukwa uli wopeledwa bwino, Tidziwa tonse kuti fodya wa mtundu uyu uli woipa ku bongo. Umapita mphuno ndi kuyenda ku bongo ndipo umafuwilitsa maso a wokokayo. Caciwiri, anthu amene amakoka fodya uyu athila mata pansi nthawi zambiri. Ndipo mata awa amene amakhala akuda amacokera mkamwa. Ndipo kucita ici, sikuonetsa kusamala mathupi bwino ai maka maka ku mabanja a Cikristu.

II. Fodya wa Sigareti (Mshanga)

Tikhoza kukonda fodya wa mtundu uyu ndipo coturukamo ciri monga munthu amene amanga nyumba yace yabwino nakonza



Mpulumutsi wawo. Kuonetsa m'mene anakhalira okondwera anayimba nyimbo zotamanda Mulungu.

1. Mariya anayimba nyimbo yotamanda Mulungu wace mwamsanga pomwe atamva kuti adzakhala mai wa Yesu pa dziko lapansi, Werengani Luka 1;46-56.

2. Angelo anayimba nyimbo kutamanda Mulungu pomwe analankhula za kubadwa kwa Yesu kwa a busa amene anali kuyangana za nkhosa nthawi ya usiku. Werengani Luka 2:14.

3. Mwamuna wokalamba, wochedwa Simion anayimba nyimbo kutamanda Mulungu pomwe anaona mwana Yesu mu kacisi. Werengani Luka 2:29-32.

NYIMBO PA NTHAWI YA ULALIKI WA YESU

Ngakhale kuti Cipangani Catsopano sicilankhula ciri conse pa za kuyimba nyimbo zotamanda Mulungu mnthawi ya Ambuye Yesu, tidziwa mopanda kukaikira kuti Yesu sanaletse anthu kuti ayimbe nyimbo. Nthawi zambiri anali kupezeka mu masunagoge momwe anthu anali kuyimba mnthawi ya mapemphero awo a tsiku ndi tsiku.

Pa nthawi ya mmadzulo pa cakudya cotsilizira, Yesu ndi ophunzira ace anayimba nyimbo mwina mau anacokera mu buku la Masalmo amene amalankhula za imfa ya Yesu. Werengani buku la Mateyu 26:30; Masalmo 116:3-4; 118:5.

MPHUNZITSI: Mphunzitsi ayenera kufunsa mafunso ena kapena kulola ophunzira ace kuti afunse mafunso.

PHUNZIRO 7

KULEMEKEZA MULUNGU KUPYOLERA MKUYIMBA NYIMBO KULINGANA NDI CIPANGANO CATSOPANO

MAU A MULUNGU: Luka 1:46-56; Luka 2:29, Mateyu 26:26; Macitidwe 16:25; Cibvumbulutso 7:9-12; 15:3-4.

MAU APAMTIMA: *"Ulemelero ukhale kwa Mulungu Kumwambamwamba, Ndi mtendere pansi pano mwa anthu amene akondwera nao."*

*(Luka 2:14)*

MAU OYAMBA:

Mu mpingo wa Baptist ndi mipingo ina yace, Akristu amakonda kuyimba nyimbo pa nthawi ya mapemphero. Ciri kuonetsa kuti nthawi ya mapemphero ndi nthawi ya padela yakuyamika Mulungu ndi nyimbo. Mamembala a nkhwaya ndi a mpingo amakondwa nako kuyimba.

Mphunziro lalero, tifuna kuti tione ndi cifukwa ninji kuyimba nyimbo mu mpingo kuli koyenera, kulingana ndi kalankhulidwe ka Cipangano Catsopano.

NYIMBO PA NTHAWI YOMWE YESU ANABADWA

Pa nthawi yomwe Yesu anabadwa, kunali cikondwelero pakati pa iwo amene analandila nkhani Yabwino pa za kubadwa kwa Yesu,



zipupa zace bwino ndipo imadetsedwa pamwamba ndi utsi ngati mwini nyumba amagwiritsa nchito nkhuni mnyumbayo. Coturuka kucokera ku moto wa nkhuni ndi cakuti utsi umadetsa zipupa, tsidwi ndi ciri conse comwe cicitika ku mapmapu kwa iye amene amakoka fodya. Coturuka mu kukoka fodya nthawi zambiri cimakhala imfa.

Pa nthawi ino tonse tidziwa kuti mtengo wa fodya uli wokwela. Munthu pa kugula fodya wa sigareti amakaikila ndi kuona kuti kapena ciri coyenera kapena ai. Mosakaikila, tiyenera kudziwa kuti pamene tikoleza fodya ndi machisa kapena ndi moto uli wonse, ife timatentha ndalama zathu ndi motowo. Ngati tikoka fodya womwe uli kugulidwa pa mtengo wa 50 Ngwee, tsono tiyenera kudziwa kuti tatentha 50 Ngwee yathu. Ena amaononga monga K1.00 kapena K2.00 pa tsiku limodzi kamba kakukoka fodya wambiri pa nthawi imodzi. Pakusiliza kwa mwezi uli wonse, amakumbukira tsono kuti sanagwiritse bwino nchito ndalama zawo zomwe zikanagwiritsidwa nchito kugula cakudya ca banja.

III. Chamba

Chamba ndi fodya wina woipa kwambiri. Pamene munthu atatha kukoka chamba, amakhala ndi mkhalidwe womvetsa manyazi. Anthu ena amafoka pomwe atatha kukoka chamba. Ena amadya kwambiri cakudya ndipo amaseka seka popanda cinthu ciri conse, amakalipa palibe kanthu ndipo amacita zinthu zomwe zibweza ulemu wawo kumbuyo. Ngati fodya wa chamba wafika ku bongo anthu ena amakhala zitsiru ndipo ena amafuntha. Koma ambiri amafuntha.

Matenda akufuntha ambiri amacokera kukukoka chamba.

Boma la Zambia ndi maboma ena akunja amaletsa kapangidwe ka chamba. Munthu aliyense amene apezedwa ndi chamba amalangidwa ndi boma iye yekha. Munthuyo akhoza kulangidwa ndi kuikidwa mndende kwa nthawi yaitali mwina akhoza kulipila ndalama. Tsono Mkristu aliyense amene acita ici amaswa lamulo la boma timacita cimodzi modzi kapena kupeza mlandu ku lamulo la Mulungu. Mwa zonse tiyeni titsilize kuti zinthu zonse zoipa zomwe zalembedwa sizingathe kuonetsa zizindikilo zabwino za Mkristu kwa munthu aliyense amene amakoka chamba. Tiyenera kukhala a ngwiro. Werengani Aroma 12:1. Mphunzitsi ayenera kulola ophunzira ace kuti alankhula pa zoipa zomwe zimaturuka mkukoka fodya wa chamba.

KODI PHUNZIRO IRI LITIPHUNZITSA CIANI?

1. Monga Akristu tiyenera kuona kuti sitipereka ife eni kukukoka fodya uli wonse kapena chamba. Ciri coipa kukoka fodya ndipo Buku Lopatulika liticenjeza kuti sitiyenera kuononga mathupi athu popeza kuti ali kacisi wa Mzimu Woyera wa Mulungu. Werengani 1 Akorinto 6:19-20.

2. Kukoka chamba ndi kuswa lamulo la boma. Ngati Mkristu akuswa lamulo la boma, sangakhale Mkristu womvera.



3. Popeza kuti tiri Akristu, ndi nchito yathu yakuti tiphunzitse anthu ena ndi ana athu, kuti akhulupirire mwa Yesu Kristu Ambuye wathu monga Mpulumutsi wawo ndipo ndi munthu mmodzi yekha amene angathe kutithandiza kuti tipambane mayesero amene angathe kutitsogolera ku njira za ucimo monga kukoka fodya.

4. Anthu ambiri amalankhula kuti ciri cobvuta kweni kweni kuleka kukoka fodya. Koma tidziwa kuti "Ndi Mulungu palibe ciri conse cobvuta." ndi cifukwa cace wokhulupirira aliyense akhoza kupambana bvuto iri. Werengani Marko 10:27.

MAFUNSO:

1. Monga Akristu, kodi cimakhala cisanzo cabwino ngati tizipereka kukukoka fodya wa mtundu uli wonse?

2. Kodi ciri cabwino kunama anthu kuti sitikoka fodya pamene tikoka fodya?

3. Monga Akristu, kodi ciri cabwino kugulitsa fodya kapena chamba?

4. Anthu ena amati kukoka fodya wa chamba umawapanga iwo kukhala a nzeru, kodi tinganene kuti mbari ya nzeru imene titenga titatha kukoka chamba icokera kwa Mulungu?